Baibulo ya ana
Ikupasilani

Danieli Wogwidwa

Yolembedwa ndi: Edward Hughes

Yojambulidwa ndi: Jonathan Hay
Alastair Paterson

Yotengedwa ndi: Mary-Anne S.

Yotathauzidwa ndi: Tapiwa Maraira

Yo pangidwa ndi: Bible for Children
www.M1914.org

©2022 Bible for Children, Inc.
Chilolezo: Muli ndi ufulu wotenga ndi kuchurukitsa makopewa koma osagulitsa.

Danieli ndi anzake atatu anali kukhala ku Isiraeli. Tsiku lina mfumu yaikulu inadza ku dziko lakwawo ndipo inatenga anyamata onse anzeru kupita nawo ku dziko lake. Mfumuyo inali ndi dzina lalitali lalitali, Nebukadinezara, ndipo inkakhala ku dziko lakutali lotchedwa Babulo.

Anyamatawa anachitiridwa bwino kwambiri ku Babulo. Mfumuyo inali itasankha anyamata abwino kwambiri ochokera m'mayiko onse padziko lapansi. Anakonza zowaphunzitsa chinenero cha ku Babulo kuti akhale atumiki ake ndi kumuthandiza kulamulira ufumu.

Chakudya nachonso chinali chabwino. Anyamatawo anadya zimene mfumu inadya. Koma Danieli ndi anzake sanafune kudya chakudyacho chifukwa chakuti chinali choperekedwa kwa milungu yonyenga. Danieli anali atalonjeza kuti sadzachita chilichonse chotsutsana ndi Mulungu wake. Mulungu wa Israyeli anali atalamula anthu ake kuti asamachite chilichonse ndi mafano kapena milungu yonyenga.



Danieli anapempha chilolezo kwa woyang'anira maphunziro ake kuti asadye chakudya cha mfumu. Mfumuyo ikadziwa, ikanakwiya kwambiri. Koma Mulungu anali atapanga Danieli kukhala wokondedwa ndi mwamuna ameneyu.

Iye anavomera kuti ayese Danieli ndi anzake. Kwa masiku khumi ankangodya masamba ndi kumwa madzi okha. Pakutha kwa masiku khumi, Danieli ndi anzake anaoneka athanzi koposa anyamata onse amene anadya cakudya ca mfumu. Choncho analoledwa kupitiriza ndi masamba ndi madzi.

Anyamatawa ankalemekeza Mulungu. Ndipo Mulungu adawalemekeza. Mulungu anawapatsa nzeru ndi luso la zimene anaphunzira, ndipo Danieli anali ndi nzeru zomvetsa masomphenya ndi maloto onse.

Pambuyo pa zaka zitatu za sukulu ku Babulo, anyamata onse anaperekedwa kwa Mfumu Nebukadinezara. Iye anasankha Danieli ndi anzake atatu kukhala opambana onse. Ndipotu Mfumu inapeza kuti Danieli anali ndi nzeru zambiri kuposa anzeru onse a mu ufumu wake.



Tsiku lina usiku, mfumu inalota maloto oipa. Anaitana amatsenga ake, okhulupirira nyenyezi ndi amatsenga kuti abwere kudzaima pamaso pake. Mfumuyo inati, "Ine ndalota loto, ndipo mzimu wanga ukufunitsitsa kumvetsa malotowo." Anzeruwo anayankha, "nati, Mfumu, mukhale ndi moyo kosatha!"

Mfumuyo inayankha kuti:
"Ayi, mundiuze zimene
ndalota ndi tanthauzo lake."
Mfumu inapitiriza kuti:
"Mudzalandira mphatso,
mphoto, ndi ulemu waukulu."
N'zoona kuti palibe aliyense
wa anzeruwo amene akanatha
kuuza mfumu maloto ake.

Amuna anzeru a mfumu anauza mfumu kuti: "Palibe munthu padziko lapansi amene angachite zimene mwapempha. Ndi milungu yokhayo imene ingachite zimenezi, ndipo siikhala padziko lapansi." Mfumuyo inakwiya kwambiri. + "Awononge anzeru onse a ku Babulo!" adalamula.

Ankhondowo atabwera kudzatenga Danieli, iye anauza Ariyoki kazembe wa mfumu kuti: “N’chifukwa chiyani mfumu ikuwononga anzeru onse?” Kenako Ariyoki anauza Danieli zonse zimene zinachitika. Danieli anapita kukaonana ndi mfumu. Iye anapempha nthawi yowonjezereka kuti afotokozere mfumu tanthauzo la loto lake.



Kenako Danieli anapita kunyumba kwake n'kukauza anzake onse aja, Sadirake, Mesake ndi Abedinego. Danieli sanadziwe chimene lotolo linali kapena tanthauzo lake, koma ankadziwa Winawake amene amadziwa zonse. Winawakeyo ndi Mulungu. Choncho Danieli ndi anzake anapemphera.



Mulungu anaonetsa Danieli loto ndi tanthauzo lake. Danieli anadalitsa Mulungu wakumwamba, nati, "Dzina la Mulungu lidalitsike mpaka kalekale, chifukwa nzeru ndi mphamvu ndi zake." Danieli anathamangira kwa mfumu n'kuiuza kuti: "Kumwamba kuli Mulungu amene amaulula zinsinsi." Iye anauza mfumu zimene ndalota ndi tanthauzo la lotolo.

Mfumu Nebukadinezara atamva lotolo ndi tanthauzo lake, anagwada pamaso pa Danieli n'kunena kuti: "Zoonadi Mulungu wanu ndi Mulungu wa milungu, ndi Yehova wa mafumu, ndi wovumbulutsa zinsinsi, + pakuti munatha kuulula chinsinsi chimenechi." Kenako mfumu inachititsa Danieli kukhala munthu wolemekezeka, ndipo inam'patsa mphatso zazikulu zambiri.

Anamuika kukhala wolamulira chigawo chonse cha Babulo, ndi mkulu wa anzeru onse a ku Babulo.

Danieli Wogwidwa

Nthano yochokera mu mau a Mulungu, Baibulo,

opezeka mu

Danieli 1-2

"Polowela pa mau anu pamapasa kuwala."
Masalimo 119:130

Mapeto

Nthano iyi yamBaibulo imakamba za ubwino wa Mulungu yemwe anatipanga ndipo akufuna kuti mumdziwe iye.

Mulungu amadziwa kuti tima chita zoipa, zimene zimachedwa chimo. Chilango cha uchimo ndi infa, koma Mulungu anatikonda kwambiri ndipo anatuma mwana wake yekha, Yesu, kuzatifela pamtanda ndi kunzunzika chifukwa cha machimo anu. Ndipo anaukanso kwa akufa na pita kumwamba! Ngati ukukhulupirira Yesu mupempheni akukhululukileni machimo anu, azakukhululukirani! Adzabwera kukhala nanu, ndipo muzakhala naye kunthawi zonse.

Ngati mukukhulupirira kuti izi ndizoona, nenani ichi kwa Mulungu: Ambuye Yesu, ndikhulupirira ndinu mwana wa Mulungu, ndipo munakhala munthu kundifera ine machimo yanga, ndipo mulinso ndi moyo. Chonde, lowani mmoyo mwanga ndikundi khululukira machimo anga, kuti ndikhale ndi moyo watsopano, ndipo tsiku lina ndikakhale ndiinu muyaya. Ndithandizeni kukumverani ndi kukhala mwa inu ngati mwana wanu. Ameni.

Welenga Baibulo ndi kuyankula ndi Mulungu matsiku onse!
Johane 3:16